Kodi Zoona Zenizeni za Mulungu N'zotani?—Gawo 2

Nkhaniyi yachokera m'buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* mutu 1. Bukuli likupezekanso pa www.jw.org.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso chifukwa chake mumazikhulupirira. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa kenako onani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI N'ZOTHEKA KUKHALA BWENZI LA MULUNGU?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N'chifukwa chiyani ena angayankhe kuti n'zosatheka? .....

.....

N'chifukwa chiyani ena angayankhe kuti n'zotheka? .....

.....

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani? .....

.....

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo? .....

.....

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Mulungu amafuna kuti tidziwe dzina lake komanso tiziligwiritsira ntchito.

(Werengani mutu 4 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 14-17.)

Werengani Salimo 83:18.

Kodi lembali likusonyeza bwanji kuti Mulungu amafuna kuti timudziwe?

.....

.....

.....

Kodi mungagwiritsire ntchito chitsanzo chotani pofuna kusonyeza kusiyana pakati pa dzina la udindo ndi dzina la lenileni?

.....

.....

.....

Tiyerekezere kuti bambo winawake yemwe ndi mphunzitsi, ali ndi ana komanso mkazi. Ngakhale kuti bamboyu ali ndi dzina lake lenileni, akhoza kumadziwikanso ndi mayina akuti mphunzitsi, ababa ndiponso bambo. Zimenezi n'zofanana ndi Mulungu. Ngakhale kuti ali ndi mayina ambiri audindo monga Atate, Ambuye komanso Mlengi, dzina lake lenileni ndi Yehova. Tikamva dzina lakuti limeneli, timakumbukira zonse zokhudza Mulunguyu.

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Yehova amafuna kuti timuyandikire.

(Werengani mutu 1 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 18-24.)

Werengani Machitidwe 17:27 ndi Yakobo 4:8.

Kodi malembawa akusonyeza bwanji kuti Yehova amafuna kuti tikhale naye pa ubwenzi?

.....

.....

.....

Werengani Ekisodo 34:6 ndi 1 Yohane 4:8, 16.

N'chifukwa chiyani Yehova akufuna kuti tidziwe makhalidwe ake?

.....

.....

.....

Tchulani makhalidwe a Yehova amene **amakusangalatsani?**

.....

.....

.....

Kodi zimakukhudzani bwanji mukadziwa zoti Mulungu amafuna kuti mudziwe dzina lake ndiponso kuti tikhale naye pa ubwenzi?

.....

.....

.....

.....

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA WANENA KUTI . . .

Pali Mulungu mmodzi yekha, ndiye zilibe kanthu kuti tikumutchula ndi dzina lotani.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

Ndikugwirizana nazo zoti kuli Mulungu woona mmodzi yekha. Koma ndikukhulupirira kuti n'zofunika kumagwiritsira ntchito dzina lenileni la Mulungu chifukwa . . .

.....

.....

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

.....

N'chifukwa chiyani mumakonda lemba limenelo?

.....

NGATI WINA WANENA KUTI . . .

Mulungu ndi waukali komanso wankhanza. Iye amangofuna kutilanga basi.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

Zipembedzo zambiri zimaphunzitsadi zimenezo. Koma ine ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa . . .

.....

.....

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

.....

N'chifukwa chiyani mumakonda lemba limenelo?

.....

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania